



Mpikisano wa za Luso
(Art Competition)



International
Labour
Organization

TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro,
Zaluso ndi Njira zofalitsira Mauthenga



TIMVERENI

Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

**Kulimbikitsa Ufulu wa Ana Kudzera M'maphunziro,
Zaluso ndi Njira zofalitsira Mauthenga**

Mpikisano wa za Luso

Kabukuka ndi kamodzi ka mabuku a maphunziro a TIMVERENI Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. TIMVERENI ndi maphunziro olimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zofalitsira mauthenga. Mabukuwa analembedwa mu chaka cha 2011 ngati mbali imodzi ya pulojekiti ya IPEC/ILO ndi chithandizo chochokera ku boma la Italy.

IPEC/ILO ikulimbikitsa kuti mabukuwa angathe kuyikidwa mu zilankhulo zosiyanasiyana komanso kusindikizidwanso kuti ntchito yothetsa nkhanza kwa ana ipite patsogolo. Ngati mwatanthauzira bukuli mu chinenero china kapena kusinthako mbali ina ya mabukuwa, kumbukirani kunena komwe mwatenga uthengawo ndiponso mutumizireko a ILO/IPEC mabuku kapena mbali yomwe mwasintha.

TIMVERENI – Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana. Kulimbikitsa ufulu wa ana kudzera m'maphunziro, zaluso ndi njira zina zofalitsira mauthenga, Ntchito Yolimbana ndi Mchitidwe Ogwiritsa Ntchito Ana pa dziko lonse, International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC), International Labour Office (ILO), Geneva, 2011.

ISBN N. 92-2-113 240-4

Mungathe kudziwa zambiri za TIMVERENI kuchokera ku:

International Programme on the Elimination of Child Labour (IPEC)
International Labour Office (ILO)

4, Route des Morillons, CH-1211 Geneva 22, Switzerland
Telephone: +41 22 799 77 47
Fax: +41 22 799 81 81
Email: childlabour@ilo.org
Web site: www.ilo.org/scream

Cholinga: Kutenga mbali mumpikisano wa luso la za manja kapena kukonza dongosolo lamtunduwu pamutu wokhudza mchitidwe ogwiritsa ntchito ana.



Phindu: Zimalimbikitsa maphunziro ndinso kafalitsidwe ka mauthenga kudzera muntchito za luso la za manja.

Nthawi

Milingo itatu ya maphunziro kudzanso ina yoonjezera poganizira nthawi yokonzekera ntchito za manjazi.

Chilimbikitso

Ntchito zaluso za manja ndi njira yamphamvu ndipo yothandiza kuonetsa za mavuto omwe mchitidwe wogwiritsa ntchito ana ochepa misinkhu amabweretsa kwa anthu okhudzidwa komanso kwa ena onse. Ngati mwachita kale gawo lokamba za luso loika ndi kumata pamodzi zidutswa zosiyanasiyana zazithunzi ndiponso nkhani zam'manyuzipepala, nkotheke kuti gulu lanu ladziwa kale kuti nkhani za mchitidwe wogwiritsa ntchito ana sizionekaoneka. Chifukwa cha ichi, anthu ambiri akunyalanyaza kuchitapo kanthu pa mchitidwewu.



Njirayi ndiyothandiza kupangitsa anthu kuti asiye kunyozera ndi kuyamba kuchitapo kanthu pa vutoli ndi kubweretsa nkhanizi poyera kudzera pamapepala komanso mu zoumbaumba za dongo kuti anthu azidziwe ndi kuziona kwathunthu. Mpikisano wa za luso la manja uthandiza kuti gulu la achinyamata lithandize kupereka chithunzi chomveka bwino cha mchitidwe wogwiritsa ntchito ana.

2 TIMVERENI Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

Gawo ili lamaphunziro ndi lothandiza kukulitsa kaganizidwe ka munthu ndipo ndi kolimbikitsa umodzi ndi mgwirizano wa gulu. Potsatira zochitika zonse za m'gawoli ndi kothandiza kuona muyezo wa kuthekera ndiponso makhalidwe a achinyamata amene mukugwira nawo ntchito. Luntha monga ngati la utsogoleri, mmene munthu angafalitsire mauthenga komanso kutha kusankha zoyenera kuti ena amve kapena ayi ndi zina mwazipatso zabwino zagawoli. Izi zingaoneke iwo atapemphedwa kuti ayendetse dongosolo lililonse kuyambira poyamba mpaka potsiriza akamphedwa kutero. Gawoli ndi lopatsanso msangulutso popeza luso la za manja limabweretsa zambiri zopatsa chidwi.



Chidziwitso

Gawo ili lingathe kutsatidwa nthawi iliyonse pambuyo pochita maphunziro a Mmene Mauthenga Amayambira komanso la za luso logwiritsa ntchito zoduladula za manyuzi pepala. Maphunziro a Mpikisano wa za Luso ndi otha kuima paokha ndipo mungathe kuwatsatira nthawi iliyonse imene inu mwaona kufunika kwake. Komabe, limagwirizana bwino ndi phunziro la kagwiritsidwe ntchito ka njira zosiyanasiyana zofalitsira mauthenga.

Kukonzekera Pali njira ziwiri zimene zingathe kutsatidwa:



- Mpikisano wa luso laza manjaungathe kukonzedwa pongokhudza gulu limodzi limene lasankhidwa. Izi zingathe kuyenda bwino ngati malo kapena zochitika zina zikupangitsa kuti kukhale kovuta kuti magulu onse achite nawo mpikisanowu, monga pakati pa anthu omwe asankhidwa kuti angochita maphunziro a mtundu, makamaka kumadera akumidzi.
- Mwinanso anthu a m'dera lonse angathe kupatsidwa mwayi wochita nawo mpikisanowu monga ngati pasukulu kapena kumadera a m'tauni.

Poonjezera apo, mukuyenera kuganizira mfundo iyi pkozekera kutsatira maphunzirowa.

- Posankha mitundu ya za luso imene ili yovomerezeka, kumbukirani kuti njira yogwiritsa ntchito zithunzi ndi zolembalemba zanyuzi zodulidwa ndi kumatidwa pamodzi siiyenera kugwiritsedwanso ntchito popeza yagwiritsidwa kale ntchito m'mbuyomu.

- Mpikisano uliwonse umafunika kukhala ndi “mutu” Ndiponso cholinga chake. Mafunso othandiza pa izi ndi monga awa: Kodi mpikisanowu cholinga chake ndi chiyani? Kodi achinyamata angopemphedwa kujambula chithunzi chokhudza kugwiritsa ntchito ana basi? Nanga izi zikhala zothandiza bwanji? Kodi sizingakhale zothandiza kubweretsa mutu wa chiyembekezo chimene tingakhale nacho kutsogoloku? Nanga opikisanawo angathe kupemphedwa kujambula chinthunzi chopititsa patsogolo ntchito zanu? Mukuyenera kulingalira bwino zonsezi zimene zikambidwe mwatsatanetsatane m’mutu womwe uno.

Chidziwitso

Mugawo lino mungathe kusankha dongosolo la ntchito imodzi, osati zones ziwiri. Komabe ngati gulu lanu lili lokhazikika ndipo mwakonzaz dongosolo lanulanu pagululo monga zalemberedwa ndi kuona kuti zayenda bwino, mungathe kupanga dongosolo lokhudza anthu ena a m'dera lanu omwe sali m'gulu lanulo. Izi zingathenso kukuthandizani kupeza nzeru zina ndi kudziwa zambiri zokhudza mavuto ena obwerera ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana.



Ngati muli ndi mwayi wopeza akatswiri omwe angathe kuthandiza paza luso la manjalikaya ndi pasukulu kapena kuchokera kwa anthu ena a pafupi nanu (monga ena mwa makolo) amene ali okonzeka kukuthandizani, aloleni kutero.

Chithandizo chapadera

Nkovuta kuti achinyamata ena m'gulu lanu ayambe kuonetsa luso limene ali nalo. Iwo angasowe chilimbikitso ndi chithandizo chanu. Nthawi zambiri iwo amavutika kuti aonetse zimene zili kukhosi kwao komabe akungosowa kulimbikitsidwa kuti adziwe kuti luso lao silideleredwa kapena kunyozedwa.

zingakhale zothandiza kwambiri kuti kuchita zaluso zosavuta kumvetsa monga ngati zojambula, ziboliboli zofanizira zinthu ndi zina. Ngati mungafune za luso zopitirira apa monga zoumba, zosoka, zojambula pa makina a kompyuta ndi zina ndibwino kuti mupemphe akatswiri kuti akuthandizeni. Cholinga sichofuna kuzunza komanso kulingalira mozama kwambiri za luso la za manjalo. Cholinga ndi chofuna kungopereka

Mwayi woti achinyamata athe kuonetsa zimene iwo akuganiza ndi kumva pogwiritsa njira zosiyanasiyana.

Kupeza Chithandizo ndi Mphotho



Ngati njira imodzi yobweretsa umwini pa zochitikazi, pemphani gulu lanulo kuti liyese kukapempha chithandizo ku malo amalonda ndi mabungwe omwe ali m'dera lanu kuti zikhale mphotho kwa ochita bwino pa mpikisanowu. Ena mwa mabizinesi a m'dera lanu angakhale omasuka komanso okondwa kuthandiza.

Nkofunika kwambiri kupereka malangizo a momwe angachitire izi asanachoke kupita kukapempha chithandizochi. Akuyenera kuchita izi polemba makalata ndi kuyimba lamy kuti agwirizane bwino za kukomana kwao. Ayesetse kuti nthawi zonse zikhale zokomera eni mabungwe ndi mabizinesi okomana nawo. Achinyamata adziwitsidwe bwino za zolinga za ntchitoyi ndiponso zochitika zonse ndipo athe kulongosola izi modzikhulupilira, mwaulemu ndiponso mopatsa chikoka. Iwo asakakamize anthu kuti apereke mwachipongwe. Ngati anthu ena sangathe kuthandiza pazifukwa zilizonse, iwo athe kuvomereza izi ndikupita kukayesa kwa ena. Chinthu chimodzi chofunika chimene angapindule pa kukomana ndi anthu osiyanasiyana ndi kuthandiza kuti anthu adziwe za mchitidwe wogwiritsa ntchito ana ndiponso zomwe achinyamata akuchita pofuna kuthetsa vutoli.

Amalonda onse amene angasonyeze chidwi chofuna kuthandiza alimbikitsidwe mtima kuti malonda awo atsatsidwa kwa anthu ndiponso iwo ayitanidwa patsiku la mpikisano kuti adzatenge nawo gawo pamwambo wopereka mphotho. Poonjezera apa, achinyamta agwiritse ntchito luso limene alipeza kuchokera m'maphunziro okhudza kafalitsidwe ka mauthenga ngati maphunzirowa achitika kale. Mabungwe ofalitsa mauthenga adziwe ndipo ayitanidwe kumwambowu. Anthu ochita malonda angachitenge kuti ndi cha mwayi kwambiri kuti ntchito nd katundu wao zidziwike kwa anthu ambiri. Yesani kupeza mphotho yoyamba, yachiwiri ndi yachitatu. Zili kwa gulu kuona ngati nkofunika kuika mndandanda woterewu kapena kungopereka phothozo kwa atatu ochita bwino kwambiri. Chofunika kwambiri ndi chakuti gulu ligwire ntchito yonse, kuyambira kupeza othandiza, ofalitsa mauthenga ndiponso kukonza dongosolo la mphotho.

Ngati mukukonza mpikisano wa za luso, mukuyeneranso kupeza anthu ena apadera oti agamule kuti zinthu zayenda bwanji. Uwu ndi mwayi wotianthu ozungulira dera lanu atenge nawo mbali pa ntchito yolimbana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana. Ngati pali kale anthu omwe mwawapeza kuti athandize pantchito yophunzitsa, mwina omwewo angathenso kuthandiza pantchito yogamula pa luso loonetsedwa patsikuli. Poonjezera apo, mungathe kuphatizikizapo anthu omwe apereka chithandizo kumbali ya mphotho. Izi zingathe kupangitsa anthu ochita malonda kuti adziwe zambiri za ntchito zomwe achinyamata akuchita pankhani ya mchitidwe wogwiritsa ntchito ana m'dera lao.

Kugamula pa Luso Loonetsedwa

Ngati mukulola anthu ena akunja kwa gulu lanu kuchita nawo mpikisanowu, chingakhaleenso chanzeru kusankha ena mwa mamembala a gulu lanu kuti akhale nawo pakati pa ogamula za zotsatira. Cholinga ndi chofuna kuti iwo athe kutenga udindo waukulu pantchito yao ndipo iwo akuyenera kuonanso ndi kuunika bwino ntchito\ ndi maganizo ena a luso ochokera kwa anzawo. Munjira iliyonse, iwo akuyenera kusankha ntchito zimene zikuonetsa bwino uthenga woyenera. Mungathenso kupeza achinyamata ena kuti agwire ntchitoyi. Mwachitsanzo, ngati pali pasukulu, sankhani anthu ogamula zalusoli kuchokera m'makalasi ena.




6 TIMVERENI Lekani Kugwiritsa Ntchito Ana

Zofunikira



- Mapepala ojambulapo a mtundu ndi makaka aliwonse.
- Pensulo. Chekeni ndi zolemba zamtundu uliwonse, kapena penti.
- Mabuku okhudza luso la zojambula-jambula ndiponso okhudza mchitidwe wogwiritsa ntchito kapena kuzunza ana.
- Mabukuwa ndi othandiza achinyamata kuti paokha athe kupanga maganizo ndi zithunzi zaozao.
- Chipinda kapena dera lokhala ndi malo ambiri osalala bwino. Khoma limene zonse zaluso zingathe kupachikidwa kapena kumatidwa.



Mwachidziwikire ngati mpikisanowu ukukhudza anthu ena akunja kwa gulu lanu, simungathe kuperekazonse zogwirira ntchito. Zinthu zimene zalembedwa apa ndi zomwe gulu lanu lingazisowe.

Ndondomeko Yake

Pangathe kukhala zifukwa zosiyanasiyana zokupangitsani kusankha magawo awa a maphunziro, koma cholinga chachikulu ndi kulimbikitsa achinyamata kuti athe kuzindikiritsana za mchitidwewu ndiponso kulimbikitsana kuchitapo kanthu limodzi. Pachifukwa ichi, mutu waukulu wa mpikisanowu ukhale pa mfundo yodziwitsa anthu ena kuti mchitidwe wogwiritsa ntchito ana ndi chiyani, ndiponso kuti uthetsedwe. Komabe, inu mupereke mfundo yatchututchu ndiponso kulongosola mwachidule kuti ofuna kulowa nawo mpikisanowu amvetse zoyenera kuchita pa za luso zilizonse zimene angafune kuonetsa. Njira yabwino yopezera izindi kufunsa gulu lanu kuti lipereke maganizo. Afunseni kuti apereke mutu wa mpikisano.

Zinthu zofunika ndi mfundo yaikulu, mutu wake ndiponso mau okulimbikitsani malingana ndi ntchito yanuyi

Mukapeza mutu wovomerezeka, lembani mwachidule zolongosola za mpikisanowu. Ngati mpikisanowu uli wongokhudza gulu lanu lokha, simukusowa kulemba izi koma kwa anthu akunja, mukuyenera kuwalongosolera momveka bwino zimene iwo akuyembekezeka kuchita. Pemphani odzipereka kuti akuthandizeni kulemba izi mwachidule pena podzazatsambalimodzikapena theka chabe. Alongosole momwe zilili pambali yogwiritsa ntchito ana popereka kuchuluka kwake, komanso kulongosola mavuto aakulu omwe angagwere ana, ndiponso momwe tsogolo lao lingakhudzidwire. Mmene zinthu zina monga maphunziro ndi ubwino wa umoyo wao zingakhudzidwirensa zilembedwenso momveka bwino. Motero, mukuyenera kulongosola mutu wa mpikisanowu ndiponso malamulo ake.



Zinanso zofunika kulembedwa momveka bwino ndi mndandanda wa zonse kuphatikiza masiku otseka ndi kupereka za luso zonse zampikisano. Masiku otsekera mpikisanowu asaikidwe kutsogolo kwambiri kuti chidwi cha anthu chikhale chilipobe chifukwa nyengo ikatalika kufunika kwake kwa mfundo za gawo ili la maphunzirowa kumazilala. Mphotoho zonse zimenezapezeka ndi kuikidwa pamndandanda zikuyenera kulembedwanso bwino lomwe.

Chitsanzo cha mmene izi zingalongosoleledwe chilipo kotsiriza kwa gawo lino la maphunziro kuti muthe kudziwa zoyenera kulongosola za mpikisanowu. Chonde, dziwani kuti chitsanzochi ndi chongokuthandizani kumvetsa momwe ziyenera kukhalira ndipo zili kwa inu kuona zimene zingakhale zofunika ndi zogwirizana kwa gulu lanu poganizira chikhalidwe ndi zina zotero.

Cholinga cha maphunzirowa ndi kulimbikitsa achinyamata kuti athe kumasuka (aliyense payekha-payekha) m'magulu mwao. Ngati palibe njira ina yochitira izi, mwachitsanzo kusowa kwa zipangizo, onesetsani kuti aliyense watenganawo mbali poonetsa zimene wachita ndi manja ake. Zingathekenso anthu awiri kupempha kuti agwilire ntchito pamodzi malinga ndi maganizo amene ali nao. Chofunika kwambiri ndi kutsatira ndi kuyang'ana bwino zomwe iwo akuchita panthawi imene apatsidwa kuti asachite zibwana. Ngati mungaone kuti ndi njira yosafuna kuchita kanthu pa gawo ili la maphunziro, ndibwino kuwalekanitsa chifukwa achinyamata ali ndi njira zochitira utambwali ngati atafuna kutero.

Kukonza Magulu



Gawo loyamba la zochita: Mpikisano wa za luso

Mlingo umodzi wa maphunziro pofuna kugwirizana zochita ndi kuyambapo, kuphatikizapo mlingo wina wotheadiza kuona zomwe anthu achita ndinso kugamula pa ntchitozo



Ngati mwagwirizana kuti mpikisanowu usakhudze anthu akunja kwa gulu lanu, gwiritsani ntchito mphindi khumi kukumbutsana zimene iwo aphunzira kale zokhudza mchitidwe wogwiritsa ntchito ana. Kenako kambiranani mutu waukulu wa zaluso zonse zimene iwo akuyembekezeka kuchita. Kambiranani za mitundu ya ntchito zaluso zimene zingathe kugwiritsidwa ntchito ndiponso zotsatira zimene mukuyembekezera kuona. Mwachitsanzo, kodi gulu likufuna kupanga chithunzi chachikulu cha pakhoma pofuna kupititsa patsogolo ntchito zake? Kapena cholinga ndi kufuna kupanga zithunzi za luso zachionetsero chabe kapena kuthandiza anthu a m'dera lanu kudziwa zambiri za mchitidwe wogwiritsa ntchito ana?

Mukatha kugwirizana za mitundu ya za luso zimene mukufuna, limbikitsani gulu lanu kuti liyambe ntchito yake ndipo gwirizanani za nthawi yomwe mungaisowe kuti ntchitoyi ithe. Mungathe kuwapatsa masabata angapo kuti agwire ntchitoyi panthawi zimene angagwirizane okha komanso mungathe kuonjezera milingo ina yamaphunziro yomwe inu mungathe kumawayang'anira.

Ntchito zonse zikatha, zipachikeni pakhoma m'kalasi m'mene mukugwilira ntchito ndipo pemphani anthu okuthandizani kugamula amene munapeza aja kuti azione bwino ntchito zonsezo. Pemphani kuti apereke ndemanga zao ndi cholinga chofuna kuti pakhale kukambirana kokhudza gulu lonse. Mungakhutitsidwe kuona kuti m'kati mwa gulu lanu muli maluso ochititsa chidwi.

Gawo lachiwiri la zochita: Mpikisano wa za Luso Anthu a M'dera Lanu

Mphunziro limodzi lothandiza kukonzekera mpikisanowu Phunziro limodzi kapenanso msonkhano wokhudza anthu a m'dera lanu kuti aone luso ndi kuthandiza kugamula pa zaluso zimene zalowa mumpikisano.

Ngati mwaganiza kuti mpikisanowu ukhudzenso anthu ena ozungulira dera lanu, onesetsani kuti mwafalitsa bwino mauthenga kudzera m'zikalata zopachikidwa pamalo osiyanasiyana, kuphatikiza kumalo omwe achinyamata amakomanira. Iziziyenerakuchitika panthawi yabwino. Zina mwa zimene zikalatazi zingalongosole mmene mpikisanowu wakonzedwera ndiponso tchutchutchu wa mphotho zimene zidzaperekedwe. Muye setse kupempha gulu anu kuti lithandize kulemba, kuchulukitsa ndi kugawa zikalatazi. Magulu ena a achinyamata adziwe kuti nawonso angathe kulowa nawo mumpikisanowu.

Mukamaliza kulandira ntchito zonse zolowa nawo mumpikisanowu, ntchito yogamula iyambe Itanani onse amene munawapeza kuti athandize pantchitoyi. Yesetsani kuti mpikisanowu ukhale mwambo waukulu ndipo opambana akasankhidwa, alandire mphotho zawo pamsonkhano waukulu. Iyi ndi nthawi yoti mabungwe ofalitsa mauthenga ayitanidwe pofunanso kuti mavuto a mchitidwe wogwiritsa ntchito ana adziwike kwa anthu ambiri. Kumbukirani kuthokoza mabungwe ndi a malonda amene anapereka mphotho kapena kuthandizapo munjira ina iliyonse, ngati kungatheke munyuzi kapena kudzera kumabungwe ena aliwonse ofalitsa mauthenga. Nkhaniyi mungathe kukambirana ndi gulu lanu pamene mukamaliza zokonzekera zanu.



Zoyenera Kuchita ndi Zoyenera Kupewa



- Mtima wopikisana usakhale patsogolo pazonse mu phunziroli. Cholinga ndi chofuna kulola achinyamata kuti athe kumasuka pogwiritsa ntchito luso lawo la za manja ndi zida zimene ali nazo kuti aonetse zoonza zenizeni za mavuto amene akuwaona pa mchitidwe wogwiritsa ntchito ana. Mtima wa mpikisano ukaikidwa patsogolo, muona kuti ena adziona ngati simbali yawo ndipo sangathe kuchita chilichonse chifukwa choti alibe luso la za manjali.

- Onesetsani kuti aliyense atenge nawo mbali. Achinyamata ena angathe kukhala ndi manyazi ndipo inu mugwiritse ntchito zochitikazi pofuna kuti ayambe kumasuka ndi kusiya kudzidlera.

- Onesetsani kuti achinyamata onse amene mukuwanyang'anira akonzeka bwino ndipo auzidwa zochita asanapite kwa anthu ena ku dera lanu kukapempha chithandizo chilichonse cha mpikisanowu.

- Yesetsani kuti mpikisanowu ukhaledi ndi kutha m'masiku amene akonzedwa pofuna kuti chidwi cha anthu chisazilale.



- Itanani onse amene apereka chithandizo china chilichonse ndiponso ena ofunikira a m'deralo kumwambo wogamula komanso wopereka mphoto kwa ochita bwino.

- Onesetsani kuti za luso za manja zonse zimene zalowa nawo mumpikisano muzisunge bwino ndiponso mupeze njira yoti anthu ambiri a m'dera lanu apeze mwayi woziona mwapadera.

Kukambirana komaliza

Phuziro limodzi

Gawola maphunziro la mpikisano wa za luso la za manja ndi losangalatsa kwambiri. Mosakaika achinyamata m'gulu lanu anali okondwa zedi kupeka ntchito zaozao zamanja komanso kuona zimene anzawo achita. Komanso ngati panali chikonzero choti ena akhale othandiza kugamula pa ntchitozi, iwo akuyenera kuti anali osangalala koposa. Pamene zonse zatha, khalani pansi ndi gulu lanu ndi kuonanso polingalira mozama ndi kukambirana za ntchito zonse zimene mwapachika m'makoma a chipinda chimene mukugwiritsa ntchito.

Mosakaika ena akhala ataonetsa luso losilirika kwambiri ndipo anthu onse akhala akuwayamikira ndi kuchita nawo chidwi. Nkofunika kuti ntchito iliyonse ithe kuonedwa ndi kuyamikiridwa ndi kulingaliridwa mozama podzifunsa za nkhani yeniyeni imene chithunzicho chikulankhula. Chithunzi chilichonse chikusonyeza zimene anthu amaganiza zokhudza mchitidwe wogwiritsa ntchito ana. Musadabwe kupeza zithunzi zina zomwe eni ake sanaganizire mozama pogwira ntchitoyi. Izi sizikusonyeza kuti analibe chidwi, koma kuti sanamasuke mokwanira kuti aonetse zenizeni zimene zili m'mitima ndi m'maganizo mwao. Ena mwa iwo ndi oti akhala opsyinjika ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito anawu ndi mavuto ake moti sangathe kuonetsa zenizeni zimene akuganiza chifukwa chowawidwa mitima.

Lankhulani ndi gulu kuti mumve kuti ndi zithunzi ziti zomwe iwo akuchita nazo chidwi kwambiri. Nkofunikanso kumva zifukwa zimene chithunzi chilichonse chikuwapatsa chidwi. Kodi chithunzicho chikulongosola nkhani yotani? Nanga pali mwayi woti zithunzizi zingathe kupereka chikhulupiliro? Kodi zina mwa izo zikuonetsa kuperewera kulikonse pa kamvetsedwe ka nkhani ya mchitidwe wogwiritsa ntchito ana? Nanga gulu lonse likuganiza bwanji za izi? Kodi akuzindikira kuti anzawo ena akulephera kuona ndi kudziwa zoonza zenizeni za mavutowa? Nanga akutha kuvomereza kuti anzawowo akuyenera kudziwa bwino za vutoli kuposa apa? Kodi izi tingazichite bwanji? Nanga tingachite bwanji kuti tithandize anthu kuti adziwe za mchitidwe wogwiritsa ntchito ana ndi zovuta zimene mchitidwewu umabweretsa pa ana?

Nanga tingachite chiyani? Pomaliza pa maphunzirowa, tikuyenera kubwerera ku mfundo iyi: kodi aliyense mwa ife angachite chiyani pothandiza anthu kuti adziwe za vutoli ndiponso kufuna kuti achitepo kanthu pochotsa ena mugoli la mavutowa? Kumbukirani kuti chimene tikufuna ndi kupeza achinyamata ambiri oti akhale akazembe othandiza kuonetsa anthu za kufunika kotipakhale kusintha. Choncho, iwathandize powapatsa zida ndi lusolofunika kuti udindo wodziwitsa ndi kupatsa anthu chikumbumtima chofuna kuchitapo kanthu ausenze ndithu.



Kuunika Momwe Ntchito yayendera ndi Kuchita Kalondolondo

Pa gawo lino la maphunziro, pali zinthu zingapo zimene zingaonetse kuti zinthu zayenda bwino kapena ayi. Wachinyamata aliyense akuyenera kuonetsa luso ndi kupereka masomphenya ake pa nkhani ya mchitidwe wogwiritsa ntchito ana. Mwa zina, khalidwe la munthu aliyense ndi limene lingapange masomphenya awa. Chinanso chothandiza ndi mgwirizano umene inu mwakhazikitsa pakati pa mamembala a gulu lanu pamaphunziro onse a m'mbuyomu. Pa mpikisano uliwonse umene mungakonze potsatira phunziroli, pakufunika kuti muwathandize achinyamatawo kukonzanso chionetsero cha za luso zonse zimene zinalowa mumpikisanowu.



Izi ndi zothandiza kulimbikitsa chikhulupiliro, umodzi ndi mgwirizano wa gululo. Chionetsero ngati ichi chingakhale chothandiza kwambiri chitachitika mokhudza anthu a m'dera lanu monga pa sukulu kapena pa gulu la achinyamata (youth club). Limbikitsani gulu lanu kuti likhale ndi ntchito zapadera zopezera ndalama kudzera muzogulitsa-gulitsa ngati pokonza ntenthandevu kapena zakumwa zoziziritsa kukhosi pamalo ochitira chionetserowo. Mwinanso zina mwa zaluso zingathe kugulitsidwamopikisana (*auction*). Apa anthu obwera akuyenera kudziwitsidwa kuti ndalama zonse zopezeka pamwambowo zithandiza nkondo yolimbana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana ochepa misinkhu kapena kuperekedwa kusukulu pofuna kuthandiza ana opulumutsidwa ku mchitidwewu.

Chionetsero kapena malonda a ntchito za lusozi ndi phata la ntchito yozindikiritisa anthu za mavutowa ndipo mukuyenera kupanga chotheka chilichonse kuti mabungwe ofalitsa mauthenga adziwitsidwe za izi kuti mauthenga athenso kufikira ku dziko lonse poonjezera pa dera lanulo. Ichi ndi chizindikiro choti mwachita zakupysa pamaphunzirowa ndiponso kuti ntchitoyi ipitilira m'dera lanulo. Pochita maphunziro ena okhudza mchitidwewu, ntchito za luso la manja zikhala zofunika kwambiri. Mwachitsanzo, pamene mudzifika pa maphunziro a zisudzo, zingakhale bwino kukometsera chipinda chimene mukuchitiramo ndi zithunzi zosiyanasiyana zochokera mumpikisanowu. Izi zithandiza anthu kuti amvetse bwino nkhani zomwe mukulongosola ndikuonesetsa kuti chithunzi chenicheni cha mchitidwe wogwiritsa ntchito ana chikuperekedwa.

Choncho, yesetsani kuti musunge zithunzi zonse zimene zinalowa mumpikisanowu ndiponso muzionetse kwa anthu mwapafupipafupi ngati kungatheke kutero.

Gawo lino la maphunziro ndi losavuta kumvetsa koma ndi lothandiza kwambiri kuti anthu azindikire za vuto logwiritsa ntchito ana pakati pa achinyamata. Kuonjezera apo, maphunzirowa ndi chida choti achinyamata athe kumasuka ndi kuonetsa zimene zili kukhosi kwao mozama kwambiri. Nthawi zambiri anthu amatha kukamba ndi kuonetsa zakukhosikudzera mu ntchito za luso kuposa m'kulankhula kapena m'kulemba chabe. Amaona kuti sakhala pa chiopsyeyo akasonyeza za kukhosi kwao kudzera muntchito za luso za manja kusiyana ndi m'mau okha.

Pogwira ntchito ndi achinyamata, nkofunika kuwapatsa njira zina ndi zina zoti athe kulongosola zamumtima mwao momasuka popanda kuwaika pachipsyeyo chilichonse. Njirazinso zimafunika kuti zikhale zosonyeza kuti iwo ndi opambana. Ntchito za luso la za manja zimathandiza kukwaniritsa izi. Kudzera m'maphunziro awa, achinyamata amayamba kuzindikira udindo wao pankhani yozindikiritsa anthu ndinso yothandiza kusintha zinthu. Powapatsa magawo osiyanasiyana pokonza mipisanowu monga ngati polemba zikalata zolongosola momwe uyendere, iwo amagwiritsa ntchito nzeru ndi luso limene ali nalo kwathunthu. Poonjezera apo, iwo ayambapo kudziwika kwa anthu a m'dera lao pamene akupempha chithandizo ku magulu osiyanasiyana pomwe iwo amakhala ndi mwayi wolongosola mwatsatane- tsatane za ntchito yomwe iwo akugwira ndiponso chifukwa chimene iwo akufunira chithandizo. Poteropo, iwo amakhala akuyambapo kuphunzira zambiri.

Motero pochoka pagawo lino la maphunziro, mungathe kupita pa mutu ndi gawo lililonse limene mungafune mogwirizana ndi nthawi ndi chikonzero chimene mwasankha. Mungathe kupita pa mutu wothandiza kupeka zinthu zosiyana-siyana ngati mungakhale kuti simunauchite kale.



Gawo Loyamba la Zoonjezera

Mpikisano wa za luso:

Ntchito yolimbana ndi Mchitidwe

Wogwiritsa Ntchito Ana ya TIMVERENI

(Yokonzedwa ndi Scariff Community College m'dziko la Ireland mwezi wa March 2001)

Kulongosola za Mpikisanowu

Ophunzira onse a *College* ino ndi oloedwa kulowa nawo mumpikisanowu popanda kuyang'ana misinkhu yawo. Onse olowa nawo akhale kuti ndi ophunzira pa *College* ino okha basi.

Tsiku lotsiriza kupereka ntchito zonse za luso ndi Lachisanu, pa 29 Marichi 2001, nthawi ya 12 Koloko masana. Palibe amene adzaloledwe kulowa mumpikisanowu tsikuli likadutsa. Ntchito zonse za luso ziperekedwe kwa Aphunzitsia za Luso la za Manja kapena ku Ofesi ya Sukulu ino. Aliyense akupemphedwa kulemba mooneka bwino dzina lake, keyala ndi zaka zake kuseli kwa chithunzi chimene akulowa nacho mumpikisanowu.

Zithunzi zonse zikhale zopeka nokha. Apa ndiye kuti pasakhale zinthunzi zodinda kuchokera ku zinzake kapena zongodula kwina kwake ndi kumata pamodzi. Sikofunika kuti zichite kukhale zopaka utoto (paint) komanso makaka a mitundu yosiyanasiyana. Ntchito zonse ziunikiridwa malinga ndi luso limene likuonetsedwa komanso kugwirizana kwake ndi mutu waukulu wa mpikisanowu.

Zithunzi zimene zidzakhale zopambana sizidzabwezedwa kwa eni ake.

Omwe adzaunikire ndi kugamula kupambana kwa zithunzi zonse ndi anthu asanu amene mmodzi mwa iwo ndi aphunzitsi a luso la za manja, mkulu yemwe akuyendetsa ntchitoyi ndiponso ana asukulu atatu am'chaka chachinayi omwe mayina ao adzalengezedwa. Zimene iwo adzagamule pa ochita bwino poyambilira, pachiwiri ndi pachitatu sizidzatsutsidwa ndi wina aliyense.

Mphotho zake ndi izi: Chokoleti chitatu kwa wopambana woyamba; chokoleti chiwiri kwa wachiwiri ndipo chokoleti chimodzi kwa wokhala pachitatu. Maina a opambana adzapachikidwa pasukulu pompano tsiku Lachisanu, pa 5 Epulo 2001.

Aliyense wofuna kulowa nawo mumpikisanowu ajambule chithunzi chachikulu chopachika pakhoma pamfundo ya mchitidwe wogwiritsa ntchito ana cholembedwa "TIMVERENI". Zili kwa inu kuona momwe mungachitire izi. Aliyense akupemphedwa kupereka chithunzi chake pa mfundo ya mchitidwe wogwiritsa ntchito ana munjira iliyonse imene angathe ndiponso akupemphedwa kulembapo mau kapena kupereka maganizo oti TIMVERENI.

Zithunzizi zingathe kukhala pa pepala la makaka kapena kukula kwina kuli konse, koma lisachepere pa pepala la m'bukhu lalikulu (A4).

Pansipa pali kulongosola kwatchutchutthu kwa nkhani yogwiritsa ntchito ana ndiponso TIMVERENI ngati njira yofuna kuthandiza onse ofuna kulowa nawo mumpikisanowu kumvetsa bwino mfundo zimene zikufunika.

Osankhidwa kuunikira ndi kugamula adzayang'ana mmene nkhani ya TIMVERENI yaikidwira pa chinthunzi ndiponso adzaona luso lina lapadera limene lagwiritsidwa ntchito pothandiza achinyamata kuti alingalire bwino nkhani yokhudza mchitidwe wogwiritsa ntchito ana.

Mutu Waukulu wa Mpikisano

Kugwiritsa ntchito ana ndi mchitidwe umene ukuchitika padziko lapansi umene umakakamiza ana a misinkhu yachichepere kuti agwire ntchito ndi cholinga choti apeze zofunika pamoyo wao wa tsiku ndi tsiku. Pali pafupi ana okwana mamiliyoni 245 (245,000,000) padziko lonse la pansi omwe akugwira ntchito ngati olembedwa omwe ena akugwira tsiku lonse, ena akugwira panthawi zina za patsiku; mwa anawa, mamiliyoni /zikwi zikwi 170 (170,000 000) amagwira ntchito zomwe zingaike moyo wao pachipsyezo.

Ntchito zimene anawa kugwira ndi zosiyanasiyana: za m'nyumba, usirikali, za chiwerewere, za ulimi, za migodi, zochotsa zinyalala, zomanga- manga, zoswa miyala, zomanga mauvuni a njerwa, zofufuza miyala yamtengo wapatali, ndi zina zambiri. Kusiyanana kwa mwana amene akugwira kaganyu ku dziko la Ireland ndi mwana wokakamizidwa kugwira ntchito kwagona pakuti winayo (wa ku Ireland) ali ndi ufulu wosankha kutero. Ana okakamizidwa kugwira ntchito alibe mwayi wosankha. Ayenera kugwira ntchito kuti iwo ndi mabanja awo asagone ndi njala. Iwo ataya umwana wao ndipo sangathe kupindula ndi maphunziro. Nthawi zina iwo amachotsedwa ku mabanja awo ali achichepere ndi kugulitsidwa kwa anthu ofuna antchito.

Iwo amagwira ntchito yakalavula gaga nthawi yaitali. Ndipo nthawi zambiri iwo amazunzidwa kuthupi, m'maganizo ndiponso nthawi zina kumbali ya zadama (zogonana). Iwo angathe kulumala mwa mitundu- mitundu chifukwa cholephera kupeza chakudya choyenera m'matupi awo ndiponso kulephera kugona mokwanira, komanso ntchito zolemetsa. Anawa sangathe kumvetsa zot umwana ndi chiyani.

Chimodzimodzinso, nkhani yoti fuko kapena mtundu wa anthu ndi maphunziro zimakhala zovuta kuti azimvetse ndi kuona phindu lake. Tsogolo lao limakhala lovuta kwambiri ndipo izi zimaika ana ao a mtsogolo pachipsyezo choti angathe kudzavutika. Anthu, makamaka achinyamta, akuyenera kudziwa za zovuta zoopysa kwambiri zimene mchitidwewu umabweretsa ngakhale kuti m'dziko lao mulibe vutoli. Akuyenera kudziwa za zoopsya zosasimbika za mchitidwewu ndiponso adzikhala oyipidwa kwambiri ndi kufuna kuchitapo kanthu pofuna kuthetsa vutoli. Nthawi yakwana tsopano kuti achinyamata ayime *njii* ndi kuchitapo kanthu. Akuyenera kusonyeza poyera kuipidwa kwao ndi mchitidwe wopanda chilungamowu ndi kuonesetsa kuti uthenga wao ufike kwa anthu ena.

Akuyenera kukuwa/kufuula (SCREAM) kuti dziko liwamvere zomwe akumva mthupi lawo komanso zomwe zili m'maganizo awo (TIMVERENI) ndi kuonetsa kuipidwa kwao kuti ena amve ndi kuthandiza kuchitapo kanthu kuti zinthu zisinthe.

SCREAM amaimira mau achingerezi oti *Supporting Children's Rights through Education, the Arts and the Media*. Apa ndiye pagona mutu wa ntchito yolimbana ndi mchitidwe wogwiritsa ntchito ana yomwe achinyamata a chaka chachinayi anagwira. TIMVERENI! (SCREAM) ndiye uthenga umene tikufuna kuti ufike ku dziko lililonse ndiponso kwa anthu onse pa dziko lapansi.

Ichi n'chifukwa chake tikufuna kuthandiza pa ntchito yojambula chithunzi chopereka uthenga wa ntchito.

Chithunzi chopambana chidzatumizidwa ku bungwe la *United Nations* loona za antchito la *International Labour Organization (ILO)*.

Tikupempha onse olowa nawo mumpikisanowu kuti ayesetse kusaka ndi kutulutsa maganizo ozama kuchokera mkati mwenimweni mwa zipinda za bongo wao. Ganizirani za liwu la *TIMVERENI* ndiponso kuzama kwa tanthauzo lake lonse. Kenako ganizani za mchitidwe wogwiritsa ntchito ana – kusowa mtengo wogwira, chisoni ndiponso ululu – ndipo pezani chithunzi chimene chingaonetse mfundo zimenezi mochititsa chidwi.

Zabwino zonse!

Zolembe zina

[illegible]

Zolembe zina

[illegible]



Lekani Kugwiritisa Ntchito Ana

ILO
International programme on the
Elimination of Child Labour (IPEC)

ILO/ IPEC Malawi Project
Mantino Complex
Behind Bizonowaty filling station
PO BOX 30135
Lilongwe

Tel: (+265)-0- 1 770 388/ 199/155

www.ilo.org/ipecc

ISBN 92-2-113240-4

